# CHOYAMBA, CHACHIWIRI NDI CHIKOKA CHACHITATU CHA MWANA WA MUNTHU YESU KHRISTU.

Yesu Khristu Iye mwini – wotchedwanso mwana wa munthu (*Yohane 6:27, Luka 17:30, Luka 19:10*) – adziwulula Iye mwini kachiwiri mumasiku ano kudzera muchoyamba, chachiwiri, ndi chikoka chachitatu: Ndipo zimenezo zinali kudzera mwa mneneri Malaki 4! Ife tingathe kuzindikira, choyamba, chachiwiri ndi chikoka chachitatu mu Baibulo, pakuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kunthawi zonse *(Aheberi 13:8*).

Kodi "kukoka" kumatanthauza chiyani?

| | |
|---|---|
| *Yohane Woyera 6:44,* | *"Palibe munthu angathe kubwera kwa Ine, kupatula Atate amene anatuma Ine atamukoka iye".* |
| *Yohane Woyera 12:32* | *"Ndipo Ine, ngati Ine ndikwezedwa mwamba kuchoka padziko lapansi, ndidzakokera anthu wonse kwa Ine"* |

Mulungu amakoka – kukoka! – mwa vumbulutso pamene Mwana (Mawu) akuwululidwa kwa ife mwa Atate (Mzimu wa Mulungu). [1]

Kupyola mwa choyamba ndi chikoka chachiwiri, kwa wokhulupilira wonse zinatumikiridwa, koma kupyola mu chikoka chachitatu wosankhidwa wokhawo a Mulungu ali kukokedwa (*1 Atesalonika 1:4-6*). [2]

**<u>Chikoka choyamba</u>**
(Mbalame zazing'ono)
→ Ungwiro
(Tsonga zitatu za Phiri)
[5] [6]

**<u>Kuchiritsidwa kwa wodwala</u>**
Mneneri amadziwa matenda ndi dzanja lake lamanzere. [3]
Mulungu anati kwa Iye, "Tsopano iwe udzatenga anthu ndi dzanja lawo,ndipo usaganize kalikonse, kungoyankhula khalidwe lomwe lanenedwa kwa iwe" [4]

Chikoka chachiwiri (nkhunda) → Chisomo (Tsonga zisanu za Phiri) [5] [6]

Masomphenya (Mphatso ya kuzindikira mizimu, uneneri, zinsinsi za mitima (Aheberi 4:12) ndi maganizo anawululidwa, pamene mawu anadziwonetsera wokha. [2] [5] [7] *(Luka 9:43-39; Yohane 1:43-51; Yohane 4:1-20; Yohane 6:63-66; Yohane 1:40-42)*

Chikoka chachitatu ndi

(Angelo akumwamba asanu ndi awiri) → Kumalizitsa (Tsonga zisanu ndi ziwiri zaphiri) [8] [9]

a) Kulalikira kwa wotayika, kwa iwo amene sangathe kupulumutsidwa konse. Monga basi zaka 2000 zapitazo. Iye anapita kumunsi ndipo analalikira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende, yomwe sinalape. Pamene chifundo chinaperekedwa kwa iwo, Iwo anakana chifundo, ndipo tsopano iwo ali kuyembekezera chiweruzo. [5] *2 Petro 2:4-6; 1 petro 3 :19-20*.

b) Kutsegulidwa kwa Mawu ; zinsinsi zowululidwa. Chikoka chachitatu chinali kutsegula zitsindikizo zisanu ndi ziwiri zimenezo, Kuwulula choonadi chobisidwa chomwe chatsindikizidwa, mu Mawu. [1]
Ndipo mu nkhondo ya choonadi, Mapeto awo anatayika, koma Mulungu anati iwo adzabwezeretsedwa kachiwiri mu tsiku lotsiriza. [10] [11]

Molingana ndi Chibvumbulutso 10:7, Zinsinsi zonse zapangidwa kudziwika pansi pa chikoka chachitatu; koma osati pansi pa choyamba kapena chikoka chachiwiri.

c) Kuyankhulidwa kwa Mawu; Yankhula Mawu, ndi kuyang'ana chomwe iwo amachita! – monga mu masiku a Yesu Khristu *(Marko 11:23-24)* [12] [13].
Koma pamene iwe ukhala molondola ndi kuchita molondola, ndi kupanga molondola, ndi kukhala nacho chikhulupiliro mwa

Mulungu, Satana adzanjenjemera pamene iwe wayankhula, chifukwa Mulungu analumbira pansi pa kukakamizidwa Iye adzasamalira pemphero limenelo. [14]

Ndipo pokha pokha ngati iwe uli munzere wantchito, kusunga Mawu a Mulungu, kuchita chokhacho chomwe Iye anakuuza iwe kuti uchite, kuyenda mwa madongosolo a Mulungu, iwe uli nawo ufulu kunena kwa Phiri limenelo, “Sunthidwa” Mulungu amasunga Mawu Ake. “Ngati inu munena kwa Phiri ili, “Sunthidwa,” wosakayika  mu mtima wanu, koma kukhulupilira kuti chomwe mwanena chifika pochitika, inu mukhala nacho icho chomwe mwanena ‘’Yesu ananena zimenenzo, mu Marko Woyera11:22. Ndicho Choonadi. Ine ndikudziwa ndicho Choonadi. Ndi Mawu a Mulungu, ndipo iwo amatsimikizira kuti ndi choonadi. Ife timangokhala amantha nthawi zina. Ife timafika pamalo, tili amantha Iye sangasunge Mawu amenewo. Iye adzasunga Mawu amenewo. Iye ananena adzachita izo. Tsopano, ife tikupeza kuti ndi zoona. Iye anatsimikizira izo. [15]

*Miyambo 18:21, “Imfa ndi moyo zili mu mphamvu ya lilime.*

*Yoswa 1:8-9; Miyambo 10:11; Miyambo 12:18; Yeremiya 18:18b; Salimo 140:3; Salimo 141:3; Miyambo 6:1-2; Miyambo 10:19; Miyambo 13:3.*

Mwa kuyankhula Mawu, kuwonetsera kasanu kwa Chisomo Cha Mulungu kunabwerapo;

- <u>***Chiwukitsiro***</u>: 1957 – Mneneri anadzuka ndi kuyankhula kwa nsomba yimeneyo, yitagona m’madzi yakufa kwa theka la Ora; ndipo iyo yinabwerera ku moyo ndipo yinasambirira kupita kutali [16]

| | |
|---|---|
| Yesu anachita chiyani? | *Yohane Woyera 11:43-44, Yesu anafuula ndi liwu lokweza “Lazaro, turuka! Ndipo wakufayo anaturuka….*<br>*Luka Woyera 7:11-17, Ndipo Yesu anati: “Mnyamata wang’ono, Ine ndinati kwa iwe, dzuka!” Ndipo iye amene anali wakufa anakhala Tsonga …* |

- ***Kulenga:*** 1959 – Agologolo anayankhulidwa kuti apezeke, tikuwonanso Genesisi 22:10-11, kulengedwa kwa mwana wankhosa ndi Abrahamu.

Pamene M'bale Branham anali kulingalira pa Mawu apa Marko 11:22-26 ndipo amadzifunsa yekha kuti izo zingakhale motani, kuyankhula kwa Phiri, apo Iye anabwera ndipo anati; "Yankhula izo, ndipo usakaike izo; koma chomwe wanena, zidzakhala pamenepo." [12]

Koma inu simungakhoze kuima apo mukufwanthura m'malingaliro anu ndi kunena izo, inu muyenera kuti mukhale mutadzozedwa kuti munena izo. [17]

Koma iye asanayankhule Mawu, Iye anayenera kuti adye mpukutu wa buku ili choyamba monga mneneri Ezekieli, ndiyeno Ezekieli anayenera kupita kunyumba ya Israeli ndi kulalikira Mawu a Mulungu (*Ezekieli 3:1-4; Chibvumbulutso 10:8-11).*

Chotero, nafenso tikufuna kuti tilingalire pa Mawu monga Mariya, ndi kuti tiwatengere iwo mu mtima wathu *(Luka 2:19; Akolose 3:16; Yohane 5 :24).* Musaiwale: Iye ndi Wansembe wa Mkulu wa Mawu Ake omwe-wopembedzera wa Mawu (*Aheberi 4:14-16; Aheberi 3:1-6).*

- ***Chipulumutso*** : 1959 – Ana amuna awiri a Mlongo Hattie Wright anapulumutsidwa. Iye, Mkazi wang'ono wodzichepetsa, anayankhula mawu woyenera, amene anakondweretsa Mzimu Woyera. [13] [18]

*Machitidwe 10:44-48, "Pamene Petro anali kuyankhula mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa onse a iwo amene anamva mawuwo."*

- ***Mphamvu pa zimphamvu za Chilengedwe: 1963*** – *Pa mkuntho wa chipale chofewa, kenako masiku atatu a dzuwa.* [6]

Yesu anachita chiyani? *Luka 8:22-25, "Pamenepo Iye anadzuka, ndipo anadzudzula mphepo ndi kututuma kwa madzi; ndipo izo zinaleka, ndipo panali bata."*

Chimodziimodzi, Yoswa anayankhula *"Dzuwa, yiima iwe pomwepo pa Gidiyoni, ndipo iwe, mwezi, mu chigwa cha Ajaloni!" (Yoswa 10:12-15)*

- Machilitso : 1963 – Chotupa cha Mlongo Meda Branham chinachoka, adokotala asanamugwire iye. [18]

Yesu anachita chani?

Kuyeretsa akhate: *Marko 1:40 – 45.*
Kutulutsa ziwanda ndi machiritso: *Mateyu 8:5-17*

- Chikoka Chachitatu: Pamene mphamvu yifika pachimake, penyani chikoka chachitatu chimenecho. Pamene nthawi yimeneyo yifika, pamene kufinyaku kufika m'munsi, pamenepo inu mudzawona, chomwe inu mwachiona chosakhazikika, chidzakhala chikuwonetseredwa mu chidzalo cha mphamvu yake – mpaka khonsolo iyi yidzayamba kudzimangitsa. Koma pamenepo Mulungu adzatakasa mwa ife chomwe tinalandira kale kuchokera kwa Iye. Iye adzatsanduliza Mawu ali mwa ife kukhala Mphamvu, mu nthawi yake. Mphamvu ya Mulungu ili mwa ife ili yokonzeka kwa chipulumutso chathu kuti chiwonetseredwe pa nthawi yomaliza. Iyo yidzawonetsera (*1 petro 1:5; Aefeso 3:20-21; 1 Akorinto 4:19-20).*
  Iwo akumangitsa. Ndiyeno pamene nthawi yimeneyo yifika, ndipo kupanikiza kufika pamalo pomwe inu mwapanikizidwira kunja, ndiye penyani Chikoka Chachitatu pamenepo, mwaona ndipo izo zidzakhala mwamtheradi kwa wotayika mwathunthu, koma izo zidzakhala kwa Mkwatibwi ndi mpingo (*Salmo 138:7).* [18]

- Chikoka Chachitatu chidzakhala makamaka kwa iwo womwe sangathe kusonkhanitsa chikhulupiliro kuti adzuke ndi kupeza kugwira kwa Mulungu. Mphamvu yake yimapangidwa yangwiro mu kufooka (*2 Akorinto 12:7-10).* [3]

- Chikoka Chachitatu : Masomphenya a chihema: Mneneri anaona chihema chachikulu chopambana chimene iye sanachionepo. Icho chinali chodzazidwa ndi kundandidwa paliponse ndi anthu ndipo iye anapanga kuitanira kuguwa; ndipo mazana ndi mazana a anthu anali kulira ndi kukondwerera iwo atatha kuvomereza Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi wawo. Kenako iye anawona kuwala kumeneko kukuchoka pa chihema chachikulu ichi ndi kupita pa kanyumba kakang'ono kamatabwa. Ndipo liwu linanena kwa Iye, "Ine ndidzakumana ndi iwe mkati m'menemo;

chimenecho chidzakhala chikoka chachitatu.” Mneneri anati “Chifukwa chiyani?”, Iye anati, “Sichidzakhala chowonetsera pagulu monga zina. Kodi sizinalembedwe, *pamene iwe upemphera, lowa mkati mwachipinda chako, ndipo pamene iwe watseka chitseko chako, pemphera kwa Atate ako amene ali mobisika; ndipo Atate ako amene amaona zobisika, adzakudalitsira iwe poyera” (Mateyu 6:6)* [2] [7]. Iye adzakumana ndife muchipinda chamuseri, mu malo a pemphero wobisika.

- Koma kodi inu munazindikira, mawonetserdwe onse awa a umulungu anali woperekedwa mwayekha. Mneneri anati iye sanapemphe Iye ndi kuti, :”Ambuye, mundilole ine ndichite izi, ndiyankhule zinthu izi zikhalepo, ndi kuchita zinthu izi apo.” Iye sanapemphe Iye zimenezo.Iye mwachifuniro Chake chomwe Chauzimu anabwera kwa iye ndipo anati, “Iwe pita wukachite ichi.” Koma ngati ife tingapite basi kumangoganizira ndi kungopitiliza chinthu mongoganizira kokha kuti izo zonse zikhala bwino, izo zikhala kupitilira wopanda ulamuliro. [19]
- iye anali kuimirira apo pomwe ndi kumayang’ana molunjika pa icho, ndipo ichi Ngati munena izo mongolingalira chabe , izo sizichitika. Koma ngati china chake mwa inu, kuti inu mudzozedwe kwa ntchitoyo, ndipo mukudziwa kuti izo ndi chifuniro cha Mulungu kuti muchite izo, ndipo mudzanena izo, izo zikuyenera kuchitika. [20]

- Chikoka Chahitatu mumgwirizano ndi chitsindikizo chachisanu ndi chiwiri ndi chinthu chimodzi chimene mneneri sakanatha kutanthauzira, chifukwa zinali muchiyankhulo chosadziwika. Koma chinali chikoka chachitatu chikubwera. Ndicho chifukwa chake kumwamba konse kunali chete kwa theka la ora pansi pa chitsindikizo cha chisanu ndi chiwiri (*Chibvumbulutso 8:1*). [21] Kubwera kwa Ambuye! *(1 Akorinto 15:51-58; 1 Tesalonika 4:13-17).*

  - Chikoka chachitatu ndi lupanga la Mfumu [20] [21] [22] – *Aheberi 4:12-13; Chibvumbulutso 19:11-16; Aefeso 6:17; 2 Atesalonika 2:7-8; Chibvumbulutso 1:16.*

  - Chikoka Chachitatu chimabweretsa chikhulupiliro chokwatulitsa. M’bale Branhman anati: Icho chili chopatulika kwambiri kuti Ine sindikuyenera kunena zochuluka za icho. Iye anati “Usanene kanthu ka icho. Icho chidziyankhulira kwa chokha.” Ichi chidzakhala chinthu chomwe chidzayambitse chikhulupiliro

chokwatulitsa pa kupita. Ndipo ine ndikuyenera kukhala chete kwa kanthawi pang'ono chabe.

Ine ndikudziwa chomwe chikoka chachitatu chili, ndipo ine ndikudziwa chomwe icho chinachita. Tsopano khalani wolemekeza, ingokhalani chete. Ora lifika posachedwapa, pomwe Mulungu achite zinthu zina zopambana kwa ife. [18]

- Chikoka Chachitatu chikubwera tsopano ku ungwiro.

  Izo zikubwera mu Chikoka Chachitatu chimenecho! Ife tsopano tikubwera ku ungwiro, chifukwa anthu akuyenera kubwera ku ichi ndi cholinga cha mkwatulo. Ndicho chomwe chikuwugwira iwo pakali pano, wukudikira kwa mpingo umenewo kuti ulowe mu ungwiro wa Chikhulupiliro Chokwatulitsa chimenecho. Kuyang'anira icho. Izo zimatanthauza zochuluka zakumeta kwa ine, izo zimatanthauza zochuluka kwa inu, koma palimodzi ife tikwanitsa mwa Chisomo cha Mulungu. [12]

- Mwa Chikoka Chachitatu, Mkwatibwi adzakhala Mawu a Mulungu kwa anthu, akalata wolembedwa wowerengedwa ndi anthu onse; Mawu a Mulungu woonetseredwa, mwa kunena kwina (*2 Akorinto 3:1-3).* [23]

**<u>Chifaniziro:</u>**


[1] "Iwo wodzozedwa panthawi yakumapeto." (65-0725M), ndime 261-262.
[2] "Kodi Masomphenya ndi chiyani?" (56-0408A), ndime 113-121, 133.
[3] "Musakhale ndi mantha , ndi Ine." (60-0305), ndime 2, 64.
[4] "Nyumba ya Mtsogolo." (64-0802), ndime 526.
[5] "Miyoyo ymwe Ili mu ndende Tsopano." (63-1110M), ndime 108, 114, 266-282.
[6] "Iye Amene Ali Mwa Inu." (65-1110M), ndime 104, 108, 215.
[7] "Chifukwa chiyani Anthu Ali Wogwedezeka gwedezeka?" (56-0101), ndime 30-50 tsamba 3-6.
[8] ".Kuima pakati." (63-0623M), ndime 148-154.
[9]"Kukopa." (63-0803E), ndime 142.
[10]"Kodi ichi ndi chizindikiro chamapeto, Mabwana." (62-1230E), ndime 292.
[11]"M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya."(60-1211E), ndime 95
[12]"Chikhulupiliro Changwiro." (63-0825E), ndime 17, 151-152, 184.
[13]"Mafunso ndi Mayankho pa Mzimu Woyera." (59-1219), ndime 20-22.
[14]"Kumukhulupilira Mulungu." (52-0224), ndime 150
[15]"Kutsimikizira Mawu Ake." (65-0426), ndime ,115-116.
[16]"Mulungu Kudzibisa Yekha Mukuphweka." (63-0317M), ndime 331.
[17]"Ine Ndakhala Ndikumva , Koma Tsopano Ine Ndaona." (65-1127E), ndime 128.
[18]"Yang'anani Kutali Kwa Yesu." (63-1229E), ndime 39, 43-44, 49, 93-102, 172-181.
[19]"Mafunso ndi Mayankho." (64-0823M), ndime 158-159.
[20]"Ukulirira Chiyani? Yankhula." (63-0714M), ndime 288-308.
[21]"Chitsindikizo cha Chisanu ndi Chiwiri." (630324E), ndime 299-300.

[22]”N’chiyani Chokopa pa Phiri?” (65-0725E), -ndime 133.
[23]”Kuvundukulidwa kwa Mulungu.” (64-0614M), ndime 280.

Mwala womangira wauzimu No. 38: Kuchokera ku Mawu Owuluridwa a ora lino, Osindikizidwa ndi: Gerd Rodewald, Friedenstr. 69, D-75328 Schomberg, Germany

www.biblebelievers.de, Fax: (+49) 72 35 33 06

Kukubwera m’modzi ndi Uthenga umene wulunjika ku Baibulo, ndi mofulumira ntchito ya kuzungulira Dziko lonse. Mbewu idzalowa manyuzi pepala, Mu zipangizo zowerengera, mpaka mbewu yosankhidwiratu ya Mulungu idzamva izo.

[M’bale Branham, “Mu Buku la Chikhalidwe- Dongosolo- Chiphunzitso cha Mpingo,” Tsamba 724]